

CHICHEWA

KULEMBA

KALATA

NDI

CHIMANGIRIZO

M'SUKULU ZA PULAYIMALE

ZIKOMO MASESE BANDA

0999 246 769/0991 295 167



MANEB (AREAS OF CONCENTRATION)

(100 malikisi)

- Ichi ndi chiunikiro chabe titha kuchotsa kapena kuonjezela.

Gawo A (malikisi 30)

1. Chimangirizo

KAPENA

2. Kalata
 - Kalata yamchezo
 - Kalata yantchito

Gawo B (malikisi 20)

3. Kumvetsa nkhani
 - Kuwerenga nkhani ndi kuyankha mafunso pa nkhani yawerengedwayo

Gawo C (malikisi 10)

4. Malonje
 - Kuyankha mafunso
5. Kupanga ziganizo



Gawo D (malikisi 40)

Malamulo a chiyankhulo

- Mitundu ya mawu
- Dzina
 - Mitundu ya mayina
 - Ntchito za mayina
 - Chachimuna ndi chachikazi
 - Magulu a mayina
 - Kapangidwe ka mayina (mayina aubale)
- Mlowam'malo
 - Mitundu ya alowam'malo
- Mfotokozi
 - Mitundu ya afotokozi
- Mneni
 - Mitundu ya aneni
 - Nthawi za aneni
 - Msintho wa aneni
- Muonjezi
 - Mitundu ya aonjezi
- Mlumikizi
 - Mitundu ya alumikizi
- Mperekezi
 - Mitundu ya mperekezi



- Mfuwu
 - Mitundu ya mfuwu
- Mvekero
 - Mitundu ya mvekero
- Ntchito za ‘ndi’ mchiganizo
- Zizindikiro zamkalembedwe
- Ndagi (zilapi)
- Mawu ofanana m’matanthauzo
- Mawu otsutsana m’matanthauzo
- Mawu amodzi okhala ndi matanthauzo angapo
- Chiganizo
 - Mitundu ya ziganizo
- Nsinjiro za chiyankhulo
 - Zining’a
 - Mikuluwiko/miyambi
 - Ntchedzero/zifanifani
 - Nseketso
 - Mizimbayitso



KALATA

Kalata imalembedwa ndi zolinga zodziwitsa anthu ena omwe ali kutali kapena malo akufupi za maganizo athu ofuna kulangiza, kucheza, kuchenjeza, kupempha kapena kuwafotokozela zina zake.

Mitundu ya kalata

- a) Kalata yamchezo/yaubale
- b) Kalata yantchito

KALATA YAMCHEZO (YAUBALE)

- Iyi ndi kalata yolembera munthu yemwe mukufuna kucheza naye, kupereka malangizo, kufunsa kapena kuyankhula zina zofunika.
- Kalatayi timalemba makolo, mnzathu, m'bale kapena m'nasi.

Magawo a kalata yamchezo

- a) Keyala
- b) Tsiku
- c) Malonje
- d) Chiyambi
- e) Thunthu
- f) Mathero
- g) Kutsanzika



Dongosolo la kalata yamchezo

a) Keyala imodzi

- Iyi ndi keyala ya wolembe kalata yomwe imalembedwa pamwamba papepala chakumanja.

Chitsanzo:

Kambilonjo Pulaimale Sukulu
Positi Ofesi Bokosi 11
Kaloga
Ntcheu

b) Tsiku lolembera kalata

- Limalembedwa mu mzere womaliza wa keyala
- Tikamalemba tisiye mzere umodzi

Chitsanzo

15 Okotobala, 2019.

c) Malonje

- Malonje ndi mawu oyambira nawo kalata
- Timalimba mawuwa kumanzere kwenikweni kwa pepala mosiya mzere umodzi kuchokera pamene tamalizira kulemba tsiku lolemba kalatayo
- Kalembedwe koyenera ka malonje a kalata zotere ndi aka:
‘Wokondedwa achimwene’ kapena ‘Wokondedwa Joni’ ngati mukulembela munthu mmodzi
- Mukamalemba anthu angapo monga kwa makolo mukhoza kulemba kuti ‘Okondwedwa amayi ndi abambo’ kapena ‘Okondwedwa makolo’



d) Chiyambi

- Mu ndime imeneyi timalembamo cholinga chomwe talembera kalata.
- Chiyambi chimaphatikizidwa ku ndime yoyamba

e) Thunthu

- Gawo limeneli timafotokoza mwatsanetsatane mfundo zathu
- Thunthu limakhala ndi ndime zitatu ndipo timayankha mafunso omwe tapatsidwa

f) Mathero

- Mu ndime imeneyi mumasonyeza kuti zokamba zanu muli kuzimaliza
- Mumathanso kupeleka moni
- Mathero amaphatikizidwa ku ndime yachitatu

g) Kutsanzika

- Mumatsanzika ndi mawu monga:
‘Ndine’, ‘Ndine mnzako’ kapena ‘Ndine wanu’
- Kenaka mumalemba dzina lanu loyamba lokha
- Sibwino kutsanzika motere: ‘Ndatha’, ‘Ndatha ine wanu’

Chitsanzo cha kalata yamchezo

Lembani kalata kwa makolo anu yowadziwitsa za matenda otsekula m'mimba omwe afala pasukulu yanu yogonera komweko.

Mwa zina tsatani izi polemba:

Ndime yoyamba

- Cholinga cha kalatayo
- Tsiku lomwe matendawo adayamba
- Chomwe chidayambitsa matendawo

Ndime yachiwiri

- Chiwerengero cha ophunzira omwe akudwala matendawo
- Chithandizo chomwe odwalawo adalandira

Ndime yachitatu

- Zomwe mukuchita kuti matendawo asafalenso



Kambilonjo Pulaimale Sukulu
Positi Ofesi Bokosi 11
Kaloga
Ntcheu

15 Okotobala, 2019.

Okondedwa Makolo,
Ndalembe kalatayi pofuna kukudziwitsani za matenda otsekula m'mimba omwe afala pasukulu yathu. Matendawa adayamba lachiwiri sabata yatha. Chifukwa chomwe chidayambitsa matendawa udali uve ndi utchisi omwe ophunzira timachita.

Ophunzira omwe akudwala matendawa ndi miyandamiyanda. Odwalawo apatsidwa mankhwala othandizira kuchepesa kutsekula m'mimba.

Pakadali pano tikuyesetsa kuti matendawo asafalenso potsata njira monga: kusamba m'manja tikachoka kozithandiza, kutaya zinyalala mudzenje komanso kutsuka zipatso tisanadye. Pomaliza mulandire moni, ngati nkotheke munditumizire ndalama ndigulire zipangizo zophunzirira.

Ndine mwana wanu,

Chimwemwe.



KALATA YA NTCHITO

- Iyi ndi kalata yokhudza ntchito monga za boma, makampani kapena mabungwe.
- Kalata yotele imalembedwa pakati pa bungwe ndi bungwe linzake kapena pakati pa munthu ndi bungwe kapenanso boma.
- Kalata zambiri zomwe anthu amalemba ku mabungwe kapena kuboma zimakhala zofunsira ntchito.

Kalata ya ntchito imayenera kuonetsa zinthu izi:

A. Makeyala awiri

- Keyala ya wolembe kalata kapena komwe kalata ikuchokera imalembedwa pamwamba chakumanja
- Keyala ya kumene kukupita kalata imakhala kumanzere. Keyalayi isanalembedwe timayenera kusiya mzere wosalembedwa m'musi mwa keyala yoyamba.

B. Tsiku

- Tsiku limalembedwa pansu pa keyala ya munthu wolembe kalata.
- Dzina lamwezi limalembedwa m'chichewa.

C. Malonje

- Awa ndi mawu osonyeza munthu yemwe tikumulemba kalata.
- Malonje amalembedwa kumanzere kwenikweni kwa pepala ndipo timasiya mzere umodzi kuchokera pomwe keyala yachiwiri yathera.
- Kalembedwe koyenera ka malonje awa ndi monga:



‘Wokondedwa Mfumu’

‘Wokondedwa Mkozi’

- Nthawi zambiri timayamba ndi mawu oti ‘Wokondedwa’ tikamachita malonje kwa munthu m’modzi koma tikamachita malonje kwa anthu opitilira m’modzi timati: ‘Okondedwa’.

D. Mutu wa kalata

- Timayenera kulemba mutu wa kalata iliyonse ya ntchito
- Sitiyenera kulemba chizindikiro cha mpumiro komalizira kwa mutu wa kalatayo.

E. Chiyambi

- M’ndime imeneyi imafotokoza cholinga chomwe tikulemba kalata yathu.
- Chiyambi chimaphatikizidwa ku ndime yoyamba.

F. Thunthu

- Mu ndime za thunthu timalembamo mfundo zonse zokhudza mutu wa nkhani kapena uthenga omwe tikufuna kutumiza.
- Mfundo iliyonse imakhala ndi ndime yakeyake ndipo ndime zimakhala zitatu potsatira mafunso omwe tapansidwa.

G. Mathero

- Awa ndi mawu omwe timanena potsiriza kulemba kalata.
- Ndimeyi imaphatikizana ndi ndime yachitatu.

H. Kutsanzika

- Timatsanzika ndi mawu monga: ‘Ndine’ kapena ‘Ndine wanu’.
- Kenaka muyenera kulemba mayina anu, loyamba (first name) komanso la kubanja kwanu (surname).



Chitsanzo cha kalata ya ntchito

Lembani kalata kwa Mphunzitsi wamkulu wa Mwayi Sekondale Sukulu, P.O Bokosi 5027, Ntcheu. Muwafotokozele kuti mwalephera kupita kokayamba Folomu 1.

Mwa zina tsatani izi polemba kalata yanu:

Ndime yoyamba

- Tchulani dzina ndi zaka zanu
- Kodi ndinu mnyamata kapena mtsikana
- Chaka chomwe mwasankhidwa
- Nambala yanu nthawi yomwe munkalembe mayeso

Ndime yachiwiri

- Tchulani chifukwa chomwe mwalepherera
- Mupemphe kuti akusungireni malo
- Mukuganiza kuti muyamba sukulu liti

Ndime yachitatu

- Ndani amene angakuchitireni umboni pa pempho lanu
- Chisangalalo chanu chidzakhala chotani akakusungirani malo



Kambilonjo Pulaimale Sukulu
Positi Ofesi Bokosi 11
Kaloga
Ntcheu

15 Okotobala, 2019.

Mphunzitsi Wamkulu
Ntcheu Sekondale Sukulu
Positi Ofesi Bokosi 134
Ntcheu

Wokondedwa Aphunzitsi,

KULEPHERA KUYAMBA FOLOMU 1

Cholinga chomwe ndalembera kalatayi ndimafuna kukufotokozerani kuti ndalephera kudzayamba sukulu ndipo mundisungire malo. Dzina langa ndi Sean ndipo ndili ndi zaka khumi ndi zinayi. Ndine mnyamata. Ndinasankhidwa kudzayamba Folomu 1 chaka chathachi. Ndimaphunzira ku Kambilonjo Pulayimale Sukulu. Mu nthawi yomwe ndimalemba mayeso ndidagwiritsa ntchito nambala iyi: 2013999213.

Ndidalephera kudzayamba sukulu chifukwa chosowa ndalama. Chotero ngati nkotheke ndimapempha kuti mundisungire malo. Ndikuganiza kuti zonse zikayenda bwino ndidzayamba sukulu chigawo chachiwiri.

Makolo anga komanso mphunzitsi wamkulu wa Kambilonjo Pulaimale Sukulu ndi amene angandichitire umboni. Ndidzakhala wokondwa mukandimvera pempho langa.

Ndine,
Sean Masese.



CHIMANGIRIZO

Kulemba chimangirizo ndikosiyana pang'ono ndi kalata yanchezo komanso yantchito.

Kusiyana ndi kwakuti chimangirizo sichikhala ndi keyala, tsiku, malonje ndi kutsanzika.

Chimangirizo chimayamba ndi mutu kutsatidwa ndi chiyambi, thunthu n'kuthera ndi mathero.

Chitsanzo cha chimangirizo

Lembani chimangirizo pa mutu uwu:

GULE WAKWATHU

Mwa zina tsatani izi polemba chimangirizo chanu:

Ndime yoyamba

- Dzina la gule yemwe amavinidwa kwanu
- Anthu omwe amavina guleyu
- Nyengo yomwe guleyu amavinidwa

Ndime yachiwiri

- Zovala zomwe zimavalidwa povina guleyu
- Zifukwa zovinira guleyu
- Ubwino wa guleyu

Ndime yachitatu

- Momwe mukulimbikitsira guleyu kuti apitirire



GULE WAKWATHU

Ndikufuna ndilembe chimangirizo pa mutu woti gule wakwathu. Dzina la gule yemwe amavinidwa kwathu ndi Ngoma. Anthu omwe amavina guleyu ndi amayi ndi abambo. Nyengo yomwe guleyu amavinidwa ndi nyengo ina iliyonse imene atsogoleri aganiza kuti avinidwe.

Zovala zomwe zimavalidwa povina guleyu ndi zikopa za nyama. Zifukwa zovinira guleyu ndi zambiri kuphatikizapo kulonga mfumu yatsopano ndi ziikondwerero za ukwati. Ubwino wa guleyu ndi wakuti anthu ovina amakhala a thanzi ndi ochangamuka.

Momwe ndikulimbikitsira guleyu kuti apitirire ndi kutenga nawo mbali povina guleyu. Izi ndi zimene ndimafuna ndilembe mu chimangirizo changa.

